



*Empowered lives.  
Resilient nations.*

# Ndondomeko Yoyendetsela Ntchito Za Kusintha Kwa Nyengo M'Malawi

## M'chidule

January 2017



## **1.0 MAU OYAMBA**

Dziko la Malawi ndi limodzi mwa maiko omwe akhudzidwa kwambili ndi kusintha kwa nyengo kamba koti chuma chake chimadalira ulimi omwe umadaliranso mvula. Malawi wakhala akukumana ndi mavuto osiyanasiyana monga ndi chilala, ng'amba, mvula yochuluka ndi kusefukila kwa madzi zomwe zakhala zikuchititsa kuti ulimi usamayende bwino ndipo mapeto ake zadzetsa njala, matenda odza kamba kosowa chakudya choyenela, kutaya miyoyo komanso katundu. Mavutowa akhala akukulirakulira kuchokera m'chaha cha 1970.

Ndondomeko yothandiza kuchepetsa mavuto omwe adza kamba ka kusintha kwa nyengo cholinga chake ndi kutsogolera ntchito zomwe cholinga chake ndikuchepetsa mphweya oipa wa mlenga lenga komanso kupeza njila zomwe zingathandize pothana ndi mavuto omwe adza kamba ka kusintha kwa nyengo. Kukhadzikitsa kwa ndondomekoyi kukugwilizana ndi malingaliro komanso ndondomeko zina m'dziko lino monga ndondomeko yachiwiri ya chitukuko yotchedwa Malawi Growth and Development Strategy (MGDS II) komanso mapangano ena omwe dziko la Malawi linasainila ndi maiko akunja. Ndondomekoyi ithandiza kuti dziko lino lithe kukwanilitsa malonjezo ake pansi pa pangano la maiko onse a pa dziko la pansi lothandiza kuthetsa mavuto omwe adza kamba ka kusintha kwa nyengo (United Nations Framework Convention on Climate Change-UNFCCC), Kyoto Protocol, Paris Agreement komanso mfundo zokhadzikika za chitukuko zotchedwa Sustainable Development Goals. Ndondomekoyi inapangidwa mogwilizana ndi magulu osiyanasiyana omwe ali ndi chidwi pa nkhanayi.

## **CHOLINGA CHACHIKULU CHA NDONDOMEKOYI**

Kupititsa patsogolo mfundo zothandiza kulimbana ndi zotsatila za kusintha kwa nyengo pogwilitsa ntchito njira za makono komanso kupeleka upangili woyenera ndi cholinga chopititsa patsogolo miyoyo ya anthu.

### **3.0 ZOLINGA ZA NDONDOMEKOYI**

- Kuthana ndi mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo kudzera mu zintchito zomwe zingapangitse kuti a Malawi onse akhale ozidalira ku mavuto omwe amadza kamba kakusintha kwa nyengo;
- Kuthandiza kuchepetsa mlingo wa mipweya ya mlenga lenga kuti isakhale chiopsezo ku moyo wa anthu mu nthawi yochepa yomwe yingathandidwe kuti chitukuko ndi chilengedwe ziyende mokhazikika;
- Kuonetsetsa kuti ntchito zokhuza kusintha kwa nyengo zikhale mbali yimodzi ya ntchito, chitukuko, kugwira ntchito limodzi ndi kalondolondo wa nthambi zonse zofunikira poonetsetsa kuti palibe kusiyana pakagwilidwe ka ntchito pakati pa amayi ndi abambo; ndi
- Kuonetsetsa kuti pali mgwilizano womveka bwino pa nkhani zosiyanasiyana zomwe zimakhudza kusintha kwa nyengo kudzera mundondomeko zabwino.

### **4.0 MFUNDO ZOYENDETSERA NDONDOMEKOYI**

Ndondomekoyi idzayendetsedwa ndi mfundo zikulu zikulu zokwana khumi ndi ziwiri zomwe zili mu Malamulo a dziko lino, mfundo za maiko a pa dziko la pansi zothandiza kuchepetsa mavuto omwe adza kamba ka kusintha kwa nyengo (UNFCCC), Kyoto Protocol, Paris Agreement komanso mfundo zokhazikika za chitukuko za Sustainable Development Goals. Mfundozi zikuunika kwambili pa kuteteza kwa ufulu wa chibadwidwe wa anthu poonetsetsa kuti pasamakhale kusiyana pa pagwilidwe ka ntchito pakati pa amayi ndi abambo, mfundo zokhadzikika za chitukuko, mfundo yoti yemwe waononga chilengedwe akuyenela kulipila, kudziwa zomwe zikuchitika mdziko; kuonetsetsa kuti mibwado yomwe ikudza mtsogolo ndi yotetezedwa, kupititsa patsogolo miyoyo ya anthu osauka komanso omwe ali pa chiopsezo, komanso kuika patsogolo zofuna za anthu olumala pa ntchito yopititsa patsogolo chitukuko.

### **5.0 ZOTSATIRA ZA NDONDOMEKOYI**

- Kuchepetsa umbalambanda wa anthu ku mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo popeza njira zamakono zothetsera

mavutowa;

- Kuchepetsa mipweya yoyipa yomwe yimaononga chilengedwe;
- Kudziwitsa anthu za mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo komanso kupeza njira zochepetsera mavutowa;
- Kulimbikitsa kafukufuku, upangiri, komanso kupeza njira za makono zothetsera mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo;
- Kuonjezera ndalama zomwe zimapita ku ntchito za kusintha kwa nyengo kudzera mu ndondomeko ya chuma ya dziko lino, kupeza ndalama kuchokera ku maiko ena komanso kuonetsetsa kuti ndalama zomwe zikupita ku ntchitoyi zikugwiritsidwa ntchito moyenera; ndi
- Kuonetsetsa kuti nkhani yokhudza kusintha kwa nyengo ndi nkhani zosiyanasiyana zokhuza chitukuko zikuunikiradwa mu nthambi zofunikira za boma.

## **6.0 MAGAWO AKULU AKULU OFUNIKA PA NDONDOMEKOYI**

### 6.1 Kupeza Njira Zopherera Ku Kusintha Kwa Nyengo

Njira zopherera ku mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo zimakumana ndi zipsinjo zambiri kamba koti dzikoli limadalira zachilengedwe pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, umphawi komanso kusowa kwa upangiri woyenera ndi chuma.

Ndondomekoyi cholinga chake ndi kuchepetsa umbalambanda wa a Malawi onse komanso kuwapatsa mwayi woti anthe kugwiritsa ntchito njira zomwe akuzidziwa pothana ndi mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo. Ndondomekoyi idzathandizanso kuonetsetsa kuti amayi, asungwana komanso anthu omwe ali pa chiopsezo akugwira nawo ntchito yokonza ndondomeko komanso kupeza njira zodzitchinjirizira ku mavuto a kusintha kwa nyengo komanso kuonetsetsa kuti anthu onse atha kupherera ku mavuto omwe amadza kamba kakusintha kwa nyengo ndiponso kupititsa patsogolo ndondomeko zokhazikika zothana ndikusintha kwa nyengo.

### 6.2 Kutchinjiriza Kusintha Kwa Nyengo

Kutchinjiriza kusintha kwa nyengo ndi ntchito zomwe zimachepetsa mipweya kuti kusintha kwa nyengo kuchepe. Kudula mitengo mwachisawawa, kudalira mphamvu za chilengedwe komanso kugwiritsa ntchito malo mosinthatintha kumachepetsa kuphimba mipweya yoyipa yomwe yimayambitsa kusintha kwa nyengo.

Ndondomekoyi cholinga chake ndi kuchepetsa mipweyayi komanso kupititsa patsogolo ntchito zomwe zingathandize kuphimba mipweyayi kuti yisatuluke kukaononga nyengo kudzera mukudzalanso mitengo komanso kugwiritsa ntchito chilengedwe moyenera.

### 6.3 Kupereka Upangiri Woyenera, Maphunziro Komanso Kudziwitsa Anthu

Maphunziro ndi chida chopititsira patsogolo chitukuko komanso kupatsa mphamvu anthu osauka ndi amene sangathe kudziyankhulira okha. Ngati anthu sakudziwa mokwanira za kuthana ndi kusintha kwa nyengo nkovuta kuti angachitepo kanthu mokwanira pa ntchito zopherera komanso zotchinjiriza kusintha kwa nyengo.

Ndondomekoyi yidzapereka upangiri ku nthambi zonse pa zakusintha kwa nyengo kuti chitukuko chipite patsogolo pogwiritsa ntchito ndondomeko zamakono komanso kuthetsa kusadziwa pa nkhani za kagwiridwe kantchito ndi kuthekera pazokambirana, ndi njira zotchinjiriza mipweya yoyipa pamene chitukuko komanso chilengedwe chikupita patsogolo.

### 6.4 Kafukufuku, Njira Zamakono Komanso Kalondolondo

Dziko la Malawi limadziwa za kufunika kochita kafukufuku komanso kupeza njira zamakono zothana ndi mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo. Pakadali pano boma la Malawi lidapeza kale zofunikira kuchita zokhudzana ndi Njira zamakono.

Ndondomekoyi yidzalimbikitsa ntchito za kafukufuku komanso kupeza njira zamakono ndi kalondolondo wabwino pothana ndi kusintha kwa nyengo popeleka upangili ndi maphunziro oyenera, komanso chuma chogwirira ntchito komanso kulimbikitsa kupeza chuma komanso kuyikapo mtima kwa boma pa ntchito zamakono zomwe zasankhidwa.

### 6.5 Chuma Chothandizira Ntchito Zokhudzana Ndi Kusintha Kwa Nyengo

Podziwa kuti dziko la Malawi likukumana ndi mavuto ochuluka pa nkhani ya kusintha kwa nyengo mpofunika kuoonetsetsa kuti ndalama zochokera m'dziko muno komanso kunjira zilipo kuti zithandizire ntchitoyi. Kuyikapo mtima pothana ndi mavutowa komanso kuwalora onse ogwira ntchito zikuluzikulu ngati a mafikitale kuti agwiritse ntchito njira za makono zitha kupindula popititsa patsogolo chitukuko komanso kakhaliro ka anthu.


Ndondomekoyi yidzaonetsetsa kuti chuma chothandizira ntchito za kusintha kwa nyengo zikuyikidwa patsogolo komanso kupititsa patsogolo mgwirizano pogwira ntchito kudzera poonjezera ndalama zomwe zimapita ku ntchitoyi kudzera mu ndondomeko ya chuma, kukhazikitsa thumba lapadera lothandiza ntchitoyi, kupeza njira zopedzera ndalama kuchokera ku maiko ena komanso ku makampani omwe siaboma.

#### 6.6 Nkhani Zina Zofunika Kuunikira

Anthu omwe ali pa chiopsezo monga amayi, ana, okalamba olumala komanso a misala ndi omwe akukhudzidwa kwambiri ndi mavuto omwe amadza kamba ka kusintha kwa nyengo. Ntchito zothana ndi kusintha kwa nyengo zingakhale zopambana komanso zokhazikika ngati anthu ngati awa akutengapo mbali.

Ndondomekoyi yidzaonetsetsa kuti nkhani zokhudza kuti pasamakhale kusiyana pa kagwiridwe ka ntchito pakati pa a mayi ndi a bambo komanso anthu onse omwe amakhala pa chiopsezo ndi nkhani zokhudza chiwerengero cha anthu ndi mbali yimodzi ya ntchito zakusintha kwa nyengo ndi cholinga chochepetsa umphawi, kutetedza chilengedwe, kuthetsa kusalana komanso kukhadzikitsa ntchito zokhuza HIV ndi AIDS komanso zoonetsetsa kuti pasamakhale kusiyana pa kagwiridwe ka ntchito pakati pa amayi ndi abambo mu ntchito zonse zokhudzana ndi kusintha kwa nyengo.

## 7.0 KAYENDETSEDWE KA NDONDOMEKOYI



*Ndondomeko yoyendetsera ntchito za kusintha kwa nyengo m'dziko muno*

## 8.0 KAGWILIDWE KA NTCHITO KOMANSO KUUNIKA MOMWE NTCHITO YIKUYENDERA

Njira yapadera yomwe yidzathandize kuunikira Ndondomekoyi yakhadzikitsidwa. Njirayi yikufotokoza mfundo zomwe zikuyenera kutsatidwa komanso momwe anthu onse okhudzidwa akuyenera kutengapo mbali poonetsetsa kuti ndondomekoyi yikugwira ntchito yake.

Ka bukuka kanasanjidwa ndi thandizo lochokera ku United Nations Development Programme (UNDP) kudzera ku National Climate Change Programme (NCCP)

Mukafuna kudziwa zambiri funsani ku:

The Director,  
Environmental Affairs Department,  
Private Bag 394, Lilongwe 3, Malawi.  
Tel (265) 1 771 111, Fax (265) 1 773 379  
Email: eadinfo@nccpmw.org  
www.nccpmw.org

Kapena

Centre for Environmental Policy and Advocacy (CEPA)  
Plot LK 388, Namiwawa, Along Glyn Jones Road  
P. O. Box 1057, Blantyre, Malawi.  
Telephone: +265 212 700 104  
Website: www.cepa.org.mw  
Email: cepa@cepa.org.mw

Mafunso onse adzere kwa Mai Dorothy Tembo-Nhlema

Lasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku mabundwe awa

